Chiyambi cha Anthu Akuda Kuphunzitsa Akuda Okha Okha (ATA Introduction Course)

Chinthu chopambana chomwe tiyenera kuphunzira ndi ichi:

Zonse zomwe timadziwa za Mulungu zimapezeka m'Baibulo. Musankhulupirire chirichonse chomwe mukuphunzitsidwa kapena kumva cha Mulungu pokhapokha chitakhala kuti chikupezeka m'Baibulo. Musaphunzitse chirichonse cha Mulungu pokhapokha chitakhala kuti chikupezeka m'Baibulo.

Mbiri

1. Chiyambi

1. Mbiri yazochitika mpaka mtsogolo. Taonani m'mene Mulungu akulamulira pa zinthu zonse.

2. Vuto lathu lalikulu: Kugwa kwa munthu muuchimo

3. Yankho la Mulungu: Mphatso ya ngwiro ya Khristu

4. Kodi izi timazilandira bwanji ngati akhristu? Nanga timakhala bwanji? Ndikosavuta kulankhula kuti ndife akhristu Komati ndikovta kukhala ngati akhristu. Tiyenera kuonetsa ntchito zathu kusonyeza kuti ndife a Yesu.

5. Baibulo ndi buku la mbiri yathu; komanso mulozo wathu omwe umatithandiza kudziwa za Mulungu ndipo ndi okwanira. [18]Ndichita umboni kwa munthu aliyense wakumva mau a chinenero cha buku ili, Munthu akaonjeza pa awa, adzamuonjezera Mulungu miliri yolembedwa m'bukumu: [19]ndipo aliyense akachotsapo pa mau a buku la chinenero ichi, Mulungu adzamchotsera gawo lake pa mtengo wa moyo, ndi m'mzinda woyerawo, ndipa izi zilembedwa m'bukumu (Chibvumbulutso 22:18-19).

A. Baibulo liribe cholakwikwa chirichonse ndipo ndila ulamuliro pa mau a Mulungu alionse. Khalani okhulupilika pakhulupilira Baibulo. Tidzakhala tikuona mau a Mulungu ambiri.

B. Tidzakahala ndi nthawi yaitali tikuona Chipangano Chakale powerenga zomwe Mulungu anauza munthu za vuto lake lalikulu. Tidzakhalanso tikuwerenga zayankho lomwe Mulungu adachita pofuna kuthetsa vutolo.

C. Tidzakhala tikulankhula zayankho la Mulungu pavuto lathu la tchimo; pakuti Yesu ndiye yankho.

D. Kenako tidzakahala tikulankhula zomwe tiyenera kuyembekeza kuti tikhale akhristu ndi m'mene tingakhalire moyo okoma pamaso pa Khristu. Tingadziwe bwanji kuti ndife akhristu.

E. Tidzalankhulanso za aphunzitsi onyenga. Musamakhululipirire chirichonse mukuphunzitsidwa kapena kumva za Mulungu pokhapokha zitakhala kuti zikuchokera m'Baibulo. Musaphunzitse china chirichonse pokhapokha mutachipeza kuti chiri m'Baibulo.

6. Tidzakhala tikuona za Chipangano Chakalae kwa nthawi yaitali. Mchifukwa chiyani tidzayamba ndi Chipangano Chakale? Baibulo ndi lokwanira ndipo sitingalimvetsetse popanda Chipangano Chatsopano. Mwachitsanzo, sitingamvetsetse ilo popanda Chipangano Chatsopano. Mwachitsanzo sitingamvetestse zakusowa kwathu Khristu popanda Chipangano Chakale. Timaona ziphunzitso za Baibulo kuti zikuyambira m'Chipangano Chakale ndipo maganizo amenewa akupitirizidwa m'Chipangano Chatsopano. Mwachitsanzo, timaona ziphunzitso zambiri m'Buku la Yesaya zokhudza ulamuliro wa Mulungu ndipo timaonanso izi m'Buku la Aroma ndipo zambiri zomwe zimapezeka m'Buku la Aroma zimachokera m'buku la Yesaya. Yesu anawerenga ndikugwiritsa Chipangano Chakale mwachitsanzo: Masalimo 22:1-18, lomwe linali Salimo la Davide. Kodi zomwe zikufotokozedwa apa ndizotani? Mateyu 27:46.

A. Apatu zikusonyeza chithunzi cha Yesu pa mtanda zaka zikwi mtsogolo. Izitu ndi zitsanzo zina zambiri za maulosi a Yesu m'Chapangano Chakale (Yesaya 42:1-9 kapena 52:13 -53:1-12 kapena Zachariya 9:9). Chipangano Chakale chinafotokoza mwatsatanetsatane za Yesu ndi chifukwa chomwe ife tiyenera kumufunira Iye.

7. Mbiri yonse yazochitika imatsogozedwa ndi Mulungu (Yesaya 45:7).

8. Chiombolo ndi phunziro lalikulu m'Chipanagano Chakale, komanso m'Baibulo. Baibulo m'Chipangano Chakale limalozera kwa Yesu Khristu ndi chiombolo chake (Masalimo 22, Yesaya 7:14).

A. Gawo lirilonse la m'Baibulo limaphunzitsa za Yesu ndi ntchito yake yachipulumutso ndikuti iye ndi maziko enieni a Baibulo. Chipangano Chakale chimafotokoza za Chipangano Chatsopano ndipo Chipangano Chatsopano chimafotokoza za Yesu Khristu; mbiri yonse imakhala ya Yesu. Tikhoza kunena kuti ngakhale Mau onse si uthenga wabwino, komatu Mau onse a Mulungu amagwirizana ndi Uthenga wabwino. Chiphunzitso komanso uthenga wina ulionse uyenera kuyang'ana kwa Yesu.

9. Chipangano Chakale ndi liu lathu lero (2 Timoteo 3:16-17).

A. Baibulo likugwirabe ntchito lero lino (Aheberi 4:12). Ndikofunika kuwerenga Baibulo nthawi zonse.

II. Tiyeni tione chiyambi cha mbiri ya Chipangano Chakale.

1. Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Izi ndi zoonekeratu kotero palibenso chifukwa chokambirana, ngakhale kuti mipingo ina imakhulupilira za maganizo oti dziko lapansi linasinthika mailo lokha (Genesisi 1:1).
2. Chilengedwe chake chinali chabwino monga kumwamba, changwiro ndi chopanda tchimo (Geenesis 1:31)
3. Ichi chinali chochitika chachikulu. Tiri ndi machimo m'dziko lino lapansi. Mavuto onse a dziko lapansi akuchokera kutchimo limodzili (Genesisi 3:1-7).
4. Zotsatira za tchimo zinali chilango; nthawi zina panthawi yomweyo komanso nthawi zina chimachedwerapo (Genesisi 3:16 – 19, 23-24)
5. Mulungu amalanga tchimo.

A. Chilango china chimayambira pansi pompano. Kawirikawiri nthawi zambiri Mulungu amachotsa madalitso omwe amafuna kukupatsa. Buku la Deutronomo 32:51-52 akufotokoza kuti Mose sanaloredwe m'dziko la malonjezo chifukwa cha tchimo lake ku Meriba.

B. Osakhulupilira amalangidwa pansi pano komanso chilango chosatha akadzamwalira.

6. Tchimo limasintha chirichonse. Tiyeni tione mau a Mulungu zokhudza tchimo.

i. Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemelero wa Mulungu (Aroma 3:23)

ii. Pakuti mphoto yake ya uchimo ndi imfa, komatu mphatso ya Mulungu ndi moyo osatha mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.

III. **Tchimo ndi zotsatira zake pa munthu**

1. Tchimo limalamulira munthu osambenuka mtima, pakuti tchimo limamanga ndipo munthu amalephera kuligonjetsa.

A. Munthu osatembenuka mtima amakonda nthawi zonse kusankha tchimo ndipo samatha kusankha chabwino ndipo ndikupyolera m'mphamvu ya Mulungu yekha pamene tikhoza kuchita zinthu zabwino.

B. Anthu ndi odwala ndipo ali ndi mtima woipa.

2. Zitsanzo kuchimwa kwa munthu ndikulephera kwake kuchita zabwino kuchokera m'Baibulo ndi chilango cha Mulungu.

A. Ana oyamba a munthu m'modzi anali wakupha. Kaini anapha Abele (Genesisi 4:8). Chilango. Kupitilira kwa tchimo la munthu ndikusowa kwake chiyemebekezo kufikira Mulungu atangochimwa - Nowa, nsanja ya Babele, Sodomu ndi Gomora etc. (Genesisi 4:11 -12)

B. Ekisodo 32:4 akunena tchimo; Genesisi 32:27-28 akunena za chilango.

Uku kunali kulambira mafano ndipo tikuona m'mene anthu anagalukira Mulungu yemwe anawaombola ku ukapolo.

C. Nkhani ya Davide ndi Betisheba tikuona chigololo komanso kupha (2 Samueli 11). Chilango 2 Sam 12:1-14. Davide akudzudzulidwa pa tchimo lake ndipo akulapa. Ngakhale Davide analapa, Mulungu anamulangabe.

D. Solomoni anachimwa pambuyo pa lonjezo la Mulungu (2 Mbiri 1:7-12).

i. Tchimo la Solomoni (1 Mafumu 11:9-10). Solomoni anafunafuna chuma chambiri ndi akazi ambiri komanso milungu ina.

ii. Chilango cha Solomoni (1 Mafumu 11:11). Nthawi yomaliza ya ufumu olumikizana.

E. Manase anali mwana wa Hezekiya, mfumu yoopa Mulungu. 2 Mafumu 21:1-6 akufotokoza za tchimo la Manase ndipo tikuona chilango pa (2 Mafumu 21:10-15).

i. Kenako Manase analapa 2 Mbiri 33:1—13 ndipo Mulungu anachedwetsa chilango mpaka nthawi ina.

Pali zitsanzo zambiri. Mulungu ndi Mulungu wachilungamo ndipo nthawi zonse amalanga tchimo la munthu.

3. Chipangano Chakale ndi nkhani yopitira ya tchimo la munthu ndipo alibe chiyembekezo chakuyanjanitsidwa ku tchimo loyamba la Adamu.

A. Nowa, Nsanja ya Babelo ndi Sodomu ndi Gomora mwachitsanzo.

4. Munthu alibe chiyembekezo mwa iye yekha. Lamulo (Malamulo Khumi); Ngati munthu atamvera lamulo la Mulungu, akhoza kulungamitsidwa, komatu palibe munthu koma Yesu yekha amene anakwanitsa kumvera lamulo mwangwiro.

5. Pa nthawi imeneyo panalibe mfumu ku Israyeli. Aliyense ankachita zomwe zinkamusangalatsa pamaso pake (zaka mazana anayi za Oweruza – zaka za mdima za dziko la Israyeli.

6. Nthawi ya Mafumu

Mfumu Saulo (1 Samueli 15:11) “Kundichititsa chisoni kuti ndinaika Saulo kuti akhale mfumu; pakuti wabwelera osanditsata ine; ndipo samachita malamulo anga.”

B. Mfumu Davide

C. Mfumu Saulo

D. Mafumu onse a Israyeli

E. Mafumu Ayuda anali oipa.

7. Aneneri ananenera zamtsogolo ndikufotokozera zomwe Baibulo linkanena. Analipo ambiri ndipo ena analemba mabuku. Ena anatchulidwa m'mabuku ena, enanso sanatchulidwe maina awo (1 Mafumu 20:13).

A. Mulungu anatumiza aneneriwa kuti achenjeze anthu ndikuwaitana iwo kuti amvere Mulungu (Onani uthenga wa Yesaya).

8. Chilango cha a Babulo. Ndikubweleranso patatha zaka makumi asanu ndi awiri za ukapolo (Ezra 9:1-2).

9. Chilango cha zaka makumi asanu ndi awiri zinatsatanizana ndi kubwereranso. Anthu anapitilira kusamvera Mulungu. Kotero Chipangano Chakale chikutsekedwa ndi chenjezo ndi lonjezo (Malaki 4:1-2).

Kuonanso nkhani ya Chipangano Chakale. "Chilengede cha ngwiro," "kugwa kwake kwa munthu mu uchimo" munthu analephera kukhala mosangalatsa Mulungu" Mulungu anapereka mwayi wambiri oombola munthu" Mulungu ndi Mulungu wa chiweruzo, koma Mulungu ali ndi chikonzero chachiombolo.

IV. Komatu Mulungu ndi Mulungu wa chikondi ndi chifundo (Yohani 3:16-17).

1. Chikonzero chake pake pa munthu chinabvumbulutsidwa munthu atangochimwa. Chisomo chinaperekedwa mwachitsanzo, munthu sanafe pamalo pomwepo. Chisomo ndi kukondera kosatiyenera komwe kuli maonekedwe a Mulungu.

A. Mulungu sanadikire kufuna chithandizo; Iye anabwera kwa Adamu (Genesisi 3:8-9).

2. Poyamba lonjezo la chiombolo likuperekedwa munthu atangochimwa. Genesisi 3:15 amayang'na pa mtanda. Mulungu anakonda munthu kwambiri kotero kuti Mulungu anafunafuna munthu kuti akhazikitse ubale wake ndi Iye. Monga adachitira m'munda muja, Yesu amafunafuna ubale ndi chiyanjano chathu pamene amadza mofanana nafe ndikutilondola.

3. Mulungu ali ndi chikonzero chachiombolo cha munthu (Aefeso 1:4)

4. Mulungu amaonetsa zikonzero zake pa Genesisi 12. Abraham ndi anthu ache osankhidwa (Genesisi 12:1-). Ndime yomwe tiyenera kuloweza pa mtima.

A. Pa Genesisi 15 tikuona mapangano a Mulungu ndi munthu. Fotokozani pangano.

Kachiwiri – Chidule cha Chipangano Chakale. Munthu alibe chiyembekezo, tchimo limamtsogolera kutsutsidwa kwake, pakutero mpulumutsi amafunika. Zonsezi zikuchokera m'Chipangano Chakale ndipo muyenera kuphunzitsa Baibulo lonse.

Chipangano Chatsopano

Mulungu akuonetsa chikonzero chake changwiro ndipo pakutero Mesiya wathu akubadwa. Apa timakhala tikuona za moyo wa Yesu Khristu, momwe tingapulumutsidwire komanso momwe tingakhalire ngati akhristu. Mau amenewanso amakhala akuona zakutsogolo.

I. Zinthu zina zokhudza chiombolo. Mchifukwa chiyani ndikuona zinthu ngati izi?

1. Muyenera kuphunzitsa anthu ndikudzifufuza nokha monga 2 Akolinto 13:5; komanso ndime ina yochitsa mantha ndi Mateyu 7:21 – 23.
2. Nthawi yatha yovomereza chipulumutso (Yesaya 55:6 -7). Landirani Khristu nthawi isanathe (imfa kapena kubwera kwake kwachiwiri).
3. Fotokozani ndime zimenezi; tsimikizirani chiombolo chanu chifukwa ambiri m'mipingo timaganizira kuti zonse ziri bwino, koma sichoncho ndipo tidzadabwa tsiku la chiweruzo.
4. Timapulumutsidwa ndi ntchito za Mulungu yekha (Yesaya 44:22 ndi Aefeso 2:8-9.
5. M'chifukwa chiyani timapulumutsidwa (Yesaya 43:25)
   A. Chifukwa cha cholinga cha Mulungu
   B. Chifukwa cha chikondi Mulungu (Aroma 5:8)
6. Chipulumutso chathu m'chosatiyenera
   A. Chifukwa ndi chisankho cha mphamvu ya Mulungu yekha. Mulungu amasaknha yemwe adzayenera kupulumutsidwa. Yesaya 44:1-2 Mulungu anasankha Yakobo m'malo mwa Esau ali m'mimba (Genesisi 25:23 kapena Aroma 9:13)
   B. Tangolingalirani za moyo wa ABrahamu, kupembedza mafano, mantha ake, komatu anatchedwa bwenzi la Mulungu. Yakobo 2:23, Mulungu amapulutsa ndipo akhoza kugwiritsa ntchito wina aliyense ngakhale mtumwi ngakhale ine kapena inu palibe ali oipitsitsa amane sangapulumutsidwe.

II. **Mungapulumutsidwe bwanji, zitsanzo zochokera ku mau a Mulungu:**

1. Aroma10:9 -13.
2. Timapulumutsidwa ndi chikhulupiriro chokha osati ntchito zathu (Aefeso 2:8-9). Sitimagawana ulemerero ndi Mulungu.
   A. Ndimeyi ikutitsimikizira kuti sitigwira ntchito kuti tipulumuitsidwe (Luka 23:39-43)

3. Izitu ndi zinthu zing'onozing'ono koma nanga mchifukwa chiyani tikuzifotokoza?

   A. Ndime zambiri za Baibulo zimasonyeza kuti tiyenera kuwerenga kwambiri.

4. Funso limafunsidwa. Kodi pali anthu ena omwe ali ndichikhulupiriro koma sangapulumutsidwe?

   A. Kodi ilipo mitindu iwiri ya anthu?

      i. Osapulumutsidwa komanso onse okhala ndi chikhulupiliro chomwe sichipulumutsa.

      ii. Opulumutsidwa ndi ochita ntchito zabwino ndi akhristu ochimwa.

5. Baibulo limapereka mafunso ena omwe tiyenera kuwalingalira.

   A. Yakobo 2:14. Chipindulo ckake nchiyani, abale anga, munthu akanena, Ndili nacho chikhulupiriro, koma alibe ntchito? Kodi chikhulupilirocho chikhoza kumpulumutsa? Yakobo 2:17 – 18, Momwemonso chikhulupiriro, chikapanda kukhala nacho ntchito, chikhala chakufa m'kati mwake, Koma wina akati, Iwe uli nacho chikhulupiriro, ndipo ine ndili nazo ntchito; undionetse ine chikhulupiriro chako chopanda ntchito zako, ndipo ndipo ine ndidzakuonetsa iwe chikhulupiriro changa chotuluka m'ntchito zanga.

   B. Ziwanda zikhulupiriranso ndipo zinthunthumira; koma iwe ukhulupirira kuti Mulungu ndi m'modzi; uchita bwino (Yakobo 2:19).

   C. Herode anakhulupirira koma chikhulupiriro chake sichinali chokwanira (Machitidwe 26:27-28).

   D. Nanga ndime monga Mateyu 7:13-14, Afilipi 2:12 ndi 2 Petro 1:10?

6. Chikhulupiriro chachipulumutso chimabala:

   A. Kulapa. Muyenera kulapa machimo anu, chikhulupiriro, kusweka mtima, kusinthika kwatchulidwa koposa makumi atatu ndi asanu m'Baibulo (Machitidwe 2:38, Mateyu 3:2, Marko 1:15 ndi Luka 13:2.

   B. Chikondi/Kumvera Yohani 3:36, Luka 6:46 ndi 1 Yohane 2:3-4

   C. Ntchito Agalatiya 5:13 ndi Luka 14:26 ndi 2 Akolinto 8:5 ndi 1 Petro 4:10 ndi Aroma 12:11

7. Kuwunikanso

A. Munthu akhoza kupulumutsidwa, kenako nkumwalira ndipo nkupita kumwamba. Munthu amene ali ndi chikhulupiriro ayenera kudzifufuza yekha kuti ali ndi chikhulupiriro chachipulumutso.

III. Mumadziwa bwanji kuti munapulumutsidwa? Zizindikiro za mkhristu zimakuchenjeza kapena kukutsimikizira. Kumbukira Mateyu 7:21-23, pamene akuchenjeza Mateyu 13:24-30. Ichi ndi chiphunzitso chopambana. Mwamwayi timatsimikiziridwa kapena kuchenjezedwa potsatira:

1. Lonjezo la mau a Mulungu.

A. Yohane 3:36

B. Aroma 10:10. Musanyozetse malonjezo a mau a Mulungu.

2. Lapani. Muyenera kulapa tsiku lililonse. Kodi tsiku lirilonse mumanyamula mtanda?

3. Kodi timakonda ndi kumvera Mulungu? Deutronomo 6:4, Marko 12.

A. Kodi timakonda ndi kumvera bwanji Mulungu? (Yohane 14:15)

B. Kumvera ndi maziko enieni akukonda Mulungu osangoti maganizo okha. Kumvera ndi chifukwa chake ndili pano ngati mphunzitsi. Yesaya 6:8 akutifotokozera kuti tiyenera kuyankha kuti inde pamene taitanidwa ndi Mulungu.

4. Kodi mumakonda mau ake? Kodi mumawerenga mau ake? Masalimo 119:11, Masalimo 119:105.

A. Kodi tinavomereza kuti tiyenera kukonda Mulungu pakumumvera Iye? Kodi mumamvera bwanji?. Muyenera kum'dziwa Iye.

Baibulo ndi buku lomwe limagulitsidwa kwambiri lomwenso sirigwiritsidwa ntchito, lomwe limaikidwa pansi tsamiro komatu musamangosunga kokha, ligwiritseni ntchito pofufuzira choonadi,

5. Kodi mumatumikira Mulungu? Yakobo 2:14-18

A. "Ndidzakupemphererani" Lonjezo lobwerezedwabwerezedwa ngati patakhala kuti palibe chochitika. Pakufunika kanthu, inde kumveka ndi kudyetsa ovulazidwa.

6. Kodi mumakhulupira mwa Yesu yekha? Yohane 14:6, Njira zonse sizitsogolera kwa Mulungu ngakhale kuti akhristu ambiri amalingalira choncho.

A. Mkhristu ndi amene amaika chikhikhulupiriro chake mwa Khristu. Chikhristu ndi chipembedzo chapadera. Pakuti chimakhulupirira Yesu yekha.

B. Zikhulupiriro: Simuyenera kudzikhulupirira izo. Kodi muli nazo pakati panu?

C. Asing'anga: Kupita la Mulungu kopemphera m'mawa kenako kupitanso kwa a sing'anga a ziwanda kumadzulo. Izitu siziyenera kukhala choncho.

7. Kodi ndinu munthu osinthika? Muyenera kukhala ndi zipatso za mzimu (Agalatiya 5:22-23). Mkhristu ayenera kuzindikira kusinthika.

8. Cholinga chathu kufunafuna chilungamo cha Mulungu (2 Petro 1:5-7)

9. Moyo wa mkhristu umaonetsa umboni wa umunthu wathu watsopano (2 Akolinto 5:17)

A. Kodi mungathe kuzindkira kusinthika m'moyo wanu?

10. Kudzichepetsa (Luka 1:52)

A. Chitsanzo chochokera m'Baibulo: Mtumwi Paulo 2 Akolinto 12:7-9. Munga unathandizira kudzichepetsa kwa Paulo. Ndi ndani ayenera kukwezedwa? Yesu yekha basi.

B. Tiyenera kukhala monga Yohane m'Bapitizi (Yohane 1:27).

11. Muyenera kukhala ndi umboni. Kodi anthu amadza kwa Yesu poona m'mene inu mukukhalira kapena kodi amathawa?

A. Kodi mumasamala bwanji akazi anu? Aefeso 5:22-24, Pakuti mamuna ndiye mutu wa mkazi; monganso Khristu ndiye mutu wa Mpingo, aliyekha Mpulumutsi wa thupilo. Komatu monga Mpingo amvera Khristu, koteronso akazi amvere amuna ao m'zinthu zonse. Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Mpingo, nadzipereka yekha m'malo mwake; kuti akampatule, atayemyeretsa ndi kumsambitsa madzi ndi mau; Kuti Iye akadziikire yekha Mpingo wa ulemelero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda chilema, Koteronso amuna azikonda akazi ao a iwo okha monga ngati matupi a iwo okha. Wokonda mkazi wa iye yekha, adzikonda yekha, pakuti munthu sadana nalo thupi lake ndi kale konse; komatu alilera nalisunga, monganso Khristu Mpingo; pakuti tili ziwalo za thupi lake. Chifukwa cha ichi munthu azisiya atate wake; ndipo iwo awiri adzakhala thupi limodzi.

Chinthu chozizwitsachi ndi chachikulu ndipo ndikunena kuti chikukhudza Khristu ndi mpingo. Kotero kuti kondani akazi anu monga inu eni ndipo mkazi alemekeze mamuna wake. Osamenya mkazi wanu. Ai musatero.

B. Musaledzere (1 Akolinto 5:11)

C. Gwirani ntchito kwambiri (Yohane 9:4, 2 Atesolonika 3:11-12)

D. Khalani okhulupilika, osati abodza (Zakaliya 8:16, Akolose 3:9, kunama ndi chinthu choipa kwambiri.

12. Pemphero (2 Akolinto 1:11, Aefeso 6:18, Akolose 4:2, Kodi mumakhala ndi nthawi yaitali yopemphera? Ndi chinthu chofunika kwambiri.

13. Kodi mamakonda akhritsu anzanu? 1 Yohane 4:7 komanso ndime yonse ndi Yohane 13:35.

14. Kodi mumakonda kulambira? Masalimo 122:1 ndi Aheberi 10:25

Zilipo zizindikiro zambiri zokhala mkhristu koma kodi izi ndi chenjezo kapena chitsimikozo chabe?

IV. Tiyembekeze chiyani ngati akhristu.

1. Moyo wa thanzi, chuma kapena chipambano? Kodi izi zingapezeke m'Mau a Mulungu?

   A. Tikayang'ana mpingo ku Uganda/Malawi kodi mipingo yolemera kapena kuti akhristu akukhala m'miyoyo yovuta? Uthenga ofuna chipambano ndi chuna waononga mpingo ku ulaya komanso ofuna zisangalalo zovinavina mu mpingo.

      i. Chiphunzitso ichi chimakuchenjezani monga dokotala. Mumadziwa kuti dokotala amakupangitsani kumva ululu pokubayani singano ya makhwala.

2. Kuvutika ndi gawo lina lalikulu la Chipangano Chakale: Yembekezani mayesero, mazunzo ndi kuvutika (1 Petro 4:12-16).

3. Yembekezerani mazunzo (2 Timoteo). Pempherani inu Mpingo ozunzidwa lero lino; khalani okonzeka kukumana ndi masautso. Mpingo wa Wakale unamangika pa masautso.

4. Kondwerani pakusautsidwa. Yakobo 1:2 ndi ndime yovuta kwambiri. Yovuta kumvera.

5. Masautso ndi ofunika ku mpingo.

   A. Masautso amabweretsa chikhulupiriro chozama ndi ulemu kwa Mulungu (1 Petro 1:6-7)

   B. Amapereka mphamvu (1 Petro 5:10)

   C. Chitsanzo cha Mulungu: Yesu anazunzika pa mtanda mwachitsanzo palibe anazunzika monga Khristu.

   D. Chenjezo. Anthu ena amagwiritsa masautso ngati chowiringula chobwerera kwa Mulungu (1 Atesolonika 3:5). "Mwa ichi inenso, posalekereranso, ndinatuma

kukazindikira chikhulupiriro chanu, kuti kapena woyesa akadakuyesani, ndipo chivuto chathu chikakhala chopanda pake.”

E. Kukhala chifupi ndi Mulungu: Kumatipangitsa ife kukondwera mwa Mulungu mwachinsinsi ndi ndi moonekera (Yakobo 1:12).

F. Masautso ndi umboni wa ntchito ya Ufumu omwe ukupitirira.

G. Aheberi 12 akuphunzitsa kuti masautso ndi gawo la chidzidzulo kwa ife (Aheberi 12:5-6). Koma ngati Mulungu sadzudzula tchimo lanu loonekera mwina nkutheka simuli mbali yake.

6. Pitirizani zomwe mumayembekezera ngati akhristu, m’mene mumaganizira pa ndalama ndi chuma (Machitidwe 2:45)

7. Sitili tokha pa nkhondoyi. Tikuyembekeza thandizo (Machitidwe 1:8). Mthandizi (Mzimu Woyera).

8. Mulungu akugwiritsa mapemphero a wanthu ena kuthandiza kupilira kuti tizame mchikhulupiriro (2 Akolinto 1:11)

V. Aphunzitsi onyenga. Ichi ndi chiphunzitso china chachikulu m’Chipangano Chatsopano ndi Chakale, lomwe liri chenjezo lochokera m’mau a Mulungu. Pali aphunzitsi onyenga ambiri pakati pathu.

1. Deutronomo 13:1-5 ikutifotokozera zochita kwa aphunzitsi onyenga. Tikudziwa kuti mphunzitsi ayenera phunzitsa choonadi poyerekeza chiphunzitso chake ndi Baibulo.

2. 2 Petro 2:1-3

3. Zitsanzo za makono za chiphunzitso chabodza kungotchula zochepa chabe:

A. Kuphunzitsa kuti ubatizo umachotsa tchimo. Mipingo imaphunzitsa zimenezi.

B. Moyo wa thanzi, chuma ndi chipambano

C. Magulu ena monga Mboni za Yehova amaphunzitsa kuti Yesu si Mulungu, komanso kuti kulibe Gahena.

D. Chiphunzitso cha Mamomoni

E. Chiphunzitso chopempherera anthu polipiritsa ndalama.

F. Kukaikira ziphunzitso zenizeni za mpingo monga kubadwa kwa Yesu kwa Maliya namwaliyo. Kukhulupirira kuti njira zonse zimatitsogolera kwa Mulungu, kuphunzitsa kuti kuchotsa mimba nkoyenera komanso kudzodza abusa amathanyula monga abusa.

Werengani 2 Yohane 2:10-11 m'mene tingaphunzitsire aphunzitsi onyenga tikakumana nao.

VI. Mathero

1. Phunzitsani Baibulo ndi kulalikira Mau a Mulungu. Phunzitsani zokhazo zopezeka m'Baibulo osatinso zina.
2. Musaphunzitse maganizo anuanu pokhapokha zitakhala kuti ndemanga zake zikuthandizidwa ndi mau a Mulungu.
    A. Musaphunzitse maganizo anu
    B. Baibulo silimanena kuti "Mulungu amathandiza amene amazithandiza yekha."
3. Werengani Baibulo ndikupemphera tsiku lirilonse. Werengani kuti mumvetsetse bwino.
4. Gwiritsani Baibulo ngati chokutsogolerani pa moyo wanu komanso chotsogolera mpingo wanu.
    A. Baibulo likhoza kuphunzitsa inu komanso mpingo wanu zakulambira mwachitsanzo:
        i. Yamikani Mulungu onani (Masalimo 22:22-23)
    B. Baibulo limatiphunzitsa ife kulalikira komanso kuphunzitsa ena (Mateyu 28:18-20, Machitidwe 1:8 ndi Yesaya 6:8).

Lonjezo la mtsogolo: Yesu akubweranso posachedwa ndipo tembenukani mitima.

Chinthu chopambana kwambiri kuphunzira pa phunziro lathu ndi ichi: Zonse zomse timadziwa za Mulungu zimapezeka m'Baibulo. Musankhulupirire chirichonse chomwe mukuphunzitsidwa kapena kumva za Mulungu pokhapokha chitakhala kuti chikupezeka m'Baibulo. Musaphunzitse chirichonse cha Mulungu pokhapokhAa chitapezeka m'Baibulo.